



# ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2026 – 2027

**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE**  
Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo


**KARONGA**  
DISTRICT

## Mwachidule

Nyengo ya dzinja ya 2026-2027 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi El Niño wa mphamvu. El Niño ndi kutentha kopyola muyezo kwa madzi m'dera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific zomwe zimakhudza kagwedwe ka mvula dziko lonse.


Madera ambiri a boma la Karonga akuyembekezera kulandira **mvula ya mlingo okhazikika kapena oposerapo** mu dzinja limeneli la 2026-2027.

### October 2026



Madera ambiri kudzakhala kopanda mvula mu mweziwu. Komabe pali kuthekera kodzalandila mvula ya Chizimalupsa yamlingo wosaposera 50mm yomwe idzakhale yamphepo yamkuntho m'madera ena.


### November 2026



M'bomali tiyembekezere mvula ya mlingo oposerapo wokhazikika mumwezi wa November.

Madera ambiri akhoza kudzalandira Mvula ya mlingo wa 200mm yomwe idzakhale ya mphezi ndi mphepo ya mkuntho.


### December 2026



Mumwezi wa December, madera ambiri ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo oposerapo okhazikika wa pakati pa 200mm ndi 250mm, koma madera ena monga kwa TA Kilupula akhoza kuzalandira mvula yamlingo oposerapo 300mm.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kuyambira m'sabata yoyamba kapena yachiwiri m'mweziwu


### January 2027



Madera ambiri akuyembekezeka kulandila mvula ya mlingo okhazikika kapena yoposerapo, yokwana 200mm. Koma madera monga SC Mwakaboko, TA Kilupula, SC Mwirangombe ndi Wasambo akhoza kuzalandira mvula yamlingo wa 250 - 300mm.

Ng'amba yosaposera sabata limodzi ikuyembekezeka mu mweziwu.


### February 2027



Mlingo wa mvula okhazikika kapena kuposera apo ukuyembekezeka m'madera ambiri m'mweziwu. Mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm ikuyembekezeka kudzagwa m'madera ambiri.


Ndipo pali kuthekera kwa ng'amba yosaposera sabata limodzi mu mweziwu.

### March 2027



Mumwezi wa March, mvula ya mlingo wochepera wokhazikika yokwana 200mm ikuyembekezeka m'madera ambiri m'bomali. Koma madera monga TA Wasambo, Kilupula ndi pa Karonga boma atha kuzalandira mvula yamlingo okwana 300mm.

### April 2027



Mu mweziwu, madera ambiri ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena woposerapo ya 200mm, madera ena kumpoto kwa bomali monga TA Kilupula akhoza kuzalandira mvula yamlingo wa 300mm.

Nyengo ya mvula ikuyembekezeka kufika kumapeto sabata lachiwiri la mwezi wa April.

### DZINJA MWACHIDULE

#### Kuyamba kwa mvula yokhazikika

sabata loyamba kapena lachiwiri mu mwezi wa December

#### Ng'amba

Pali kuthekera kwa ng'amba yosaposera sabata limodzi m'miyezi ya January ndi February


#### Kutalika kwa nyengo yadzinja

Dzinja lidzakhala masiku apakati pa 110 ndi 130

#### Mathero a mvula dzinja

Sabata lachiwiri m'mwezi wa April 2027

| MONTH | NORMAL RANGE  | FORECAST |
|-------|---------------|----------|
| OCT   | 0.0 – 0.0     | 16.4     |
| NOV   | 6.5 – 56.8    | 88.8     |
| DEC   | 101.7 – 178.2 | 227.8    |
| JAN   | 135.9 – 214.3 | 184.6    |
| FEB   | 113.4 – 154.0 | 160.0    |
| MAR   | 159.5 – 266.4 | 272.2    |
| APR   | 80.8 – 184.9  | 221.4    |



Chithunzi ichi chapereka ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:



Tsatilani ulosi ndi malangizo ochokera ku nthambi yoona zanyengo



For further information contact:

The Director of Climate Change and Meteorological Services,  
P.O. Box 1808, Blantyre.



+265 991 69 00 61



metdept@metmalawi.gov.mw



www.metmalawi.gov.mw